MBIRI YA KATIKISIMU WA BAIBULO
MBIRI YA CHIPANGANO CHAKALE MWACHIDULE

Achinyamata (Kalasi yachiwiri)
Buku loyamba la awiri

Lolembedwa ndi **Rev Prof. H. C. Hoeksema**
Mkonzi ndi **Pastor J.J.Lim**
Wothathandizira wapadera ndi **David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

February 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mbiri ya Katikisimu Wa Baibulo- Mbiri ya Chipangano Chakale Mwachidule
(Ana okulilapo- Buku Loyamba la Awiri)

Lolembedwa ndi **Prof H.C. Hoeksema**
Mkonzi ndi **J.J.Lim**
Wothathandizira wapadera ndi **David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi Prof H.C. Hoeksema eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mau Oyambirira a Mlembi

Bukuli ndi lothandizira Buku la Chipangano Chatsopano lolembedwa ndi Rev G. VankenBerg. Poligwiritsa ntchito, tikuyenera kuyamba ndi mabuku a ana kudzabwera a akulu omwe ndi gawo la mabuku ano.

Kuti makolo ndi aphunzitsi adziwe zolinga ndi zomwe akuyembekezera mmaphunzirowa, tikupereka ndemanga izi:

1. Cholinga cha kabuku kano ndi kuwadziwitsa ana athu mwachidule ndi mwadongosolo zoona zenizeni za Mbiri ya Chipangano Chakale.
2. Kuti izi zitheke, sitingodalira kabuku kano kokha ndi aphunzitsi ayi, komanso kuti ana aphunzire ndi kuloweza pamtima mwa iwo wokha komanso mothandizidwa ndi makolo awo.
3. Musanyalanyaze ntchito yoti ana achite yomwe yakonzedwa mkabuku kapadera, ngati tikufuna kuti maphunzirowa akhale aphindu pomaliza pa maphunziro 25 a mkabuku kano. Kabukuka kakonzedwa mwakuti ana akhale ndi chidwi chowerenga ndime zina mBuku Lopatulika zomwe zikugwairizana ndi phunziro lirilonse.
4. Tikuvomerezanso kuti mugwiritse ntchito mapu pophunzitsa katekisimuyu.
5. Ana atha kupindula ndi mavesi oloweza pamtima. Titha kuwona zodabwitsa titachita khama komanso komanso kuwalimbikitsa aphunzitsi athu. Tisachepetse luso la wana loloweza mavesi pamtima; ndipo mavesi amenewa ndi woyenerera kwa ana a zaka 9 ndi 10.

Mulungu wathu wa chipangano atithandize kuti ana athu akhale ndi maziko abwino a Mawu ake.

- Ena mwa oyambirira omwe analemba Prof H. C. Hoeksema

Mau oyambirira a Mkonzi

Kugwiritsa ntchito Katekisimu pofuna kuphunzitsa ana aang'ono mu mpingo ndi njira yakale. Timabuku tino takonzedwa kuti tipereke chiyambi cha mbiri ya Baibulo kuti zikhale maziko a maphunzitso a katekisimu monga Katekisimu Wachidule wa Westminister. Takonza zolakwika zina mbuku lathu loyambilira, komanso mayankho ena kuti agwirizane bwino ndi mafunso.

Ana ndi makolo amene agwiritsapo ntchito buku la Kalasi Yoyamba [ana oyamba kumene] adzaona kuti buku lino likusowa kuikapo chidwi kwambiri kuposa loyambalo. Izi ziri choncho malingana ndi kamvetsedwe ka ana. Makolo ndi aphunzitsi awonetsetse kuti sakuumiriza ana ochedwa kumvetsa kuloweza ntchitoyi chimomodzi ndi ana omva msanga. Tikuganizanso kuti makolo omwe ana awo sangathe kuloweza phunziro lonse pa nthawi imodzi, agawe phunziro kangapo. Mwachitsanzo, ana atha kuphunzira mafunso awiri tsiku lirilonse pa sabata, ndi Vesi Loloweza pa Mtima, tsiku loweruka. Nditsindike zomwe ananena Prof. Hoeksema kuti: "Tisadelere luso la ana loloweza pamtima zomwe aphunzira." Nthawi zambiri timaona kuti zomwe ife akulu tikuziona kuti nzosatheka kuziloweza, ana amatha kuziloweza mosavuta ndi modabwitsa. Izi sizitanthauza kuti ana ndi makolo asagwire ntchito molimbika!

Yehova adalitse ntchito yathu ino yophunzitsa ana kuti akule mnjira yawo.

- Pastor J. J. Lim

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 1
CHILENGEDWE CHA DZIKO

1. Ndi chiyani chinachitika pa chiyambi?

Mulungu analenga dziko la kumwamba ndi la pansi pano, ndi zonse zokhalamo. (Gen 1:1-27)

2. Ndi liti pamene Mulungu analenga zithu zonse?

Zaka zosachepera 4 000 Ambuye Yesu asanabadwe.

3. Kulenga kwa dziko kunatha masiku angati?

Masiku sikisi ndipo la seveni Mulungu anapuma. (Gen 1:31 - 2:1)

4. Kodi Mulungu analenga bwanji zinthu zonse?

Ndi Mau ake a mphamvu. (Gen 1:3; onaninso mongo Ahe 11:3)

5. Kodi Mulungu analenga bwanji munthu?

Mulungu anapanga munthu kuchokera ku dothi, namuuzira mpweya wopatsa moyo m'mphuno zake. (Gen 2:7)

6. Kodi Baibulo limatiuzanso za munthu?

Mulungu adalenga muthu m'chifanizo chake, kuti amkonde ndi kumtumikira kwa thunthu.(Gen 1:26-27)

7. Kodi Mulungu anapereka ndani kwa Adamu ngati omuthandizira?

Eva, yemwe Mulungu anampanga kuchokera ku nthiti ya Adamu. (Gen 2:21-23)

8. Kodi Mulungu adamuika Adamu ndi Eva kuti?

Ku Paradizo, munda wokongola wa Edeni (Gen 2:8)

9. Kodi Adamu adaitanidwa kuti adzachite chiyani?

Ngati mfumu ya zolengedwa zonse, Adamu adaitanidwa kudzatumikira Mulungu. (Gen 2:15)

10. Kodi pachiyambi panali tchimo ndi imfa?

Ayi, Mulungu adaona kuti zonse zimene adalengazo zinali zabwino. (Gen 1:31)

*Vesi loloweza pamtima**:***

Phunzirani mabuku onse a mchipangano cha kale mundondomeko yake omwe ndi:

Genesis, Eksodo, Levitiko, Numeri, Deoteronomo, Yoswa, Oweruza, Rute, 1 Samuele, 2 Samuele, 1 Mafumu, 2 Mafumu, 1 Mbiri, 2 Mbiri, Ezara, Nehemia, Estere, Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki, Nyimbo ya Solomo, Yesaya, Yeremiya, Maliro, Ezekiele, Daniele, Hoseya, Yowele, Amosi, Obadiya, Yona, Mika, Nahumu, Habakuku, Zephaniya, Hagai, Zakariya, Malaki.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2
CHIYAMBI CHA TCHIMO

1. Kodi ndi mitengo yanji yokongola imene Mulungu adayiika m'Paradizo muja?

Mtengo wopatsa moyo ndi mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa. (Gen 2:9)

2. Kodi Adamu ndi Eva anayenera kudya zipatso za mtengo wopatsamoyo?

Inde, zipatso zake zinali chizindikiro cha moyo wosatha umene anayenera kukhala nawo. (Gen 2:16; 3:22[1])

3. Kodi anayenera kudya zipatso za Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoipa?

Ayi, popeza Mulungu anawalamula kuti asadye chipatso chirichonse cha mtengowo. (Gen 2:17)

4. Ndi ndani adamunyenga Eva kuti asamvere Mulungu ndi kudya zipatso za mtengo uja?

Satana, kudzera mwa njoka. (Gen 3:1)

5. Satana mdierekeziyo adamunyenga bwanji Eva?

Iye adati, "Kufa simudzafa konse." (Gen 3:4)

6.Kodi Eva adakhulupirira bodza la satana mdierekezi?

Inde, adadya chipatso chija, komanso adampatsanso Adamu kuti adye. (Gen 3:6)

7. Kodi Mulungu adalanga Adamu ndi Eva?

Inde, anataya ubwenzi wawo ndi Mulungu, themberero la imfa linawagwera ndi ana awo omwe. (Gen 3:8-11, 16-19; Akol 1: 21; Aga 3:10)

8. Kodi tchimo lawo lidabweretsa chiani pa dziko lapansi?

Dziko lonse lapansi lidatembereredwa.(Gen 3:17-18)

9. Kodi Mulungu adalolanso Adamu ndi Eva kudya chipatso cha Mtengo Wopatsa Moyo uja zitangochitika izi?

Ayi, Mulungu adawatulutsa mmunda muja, ndi kukawasiya kutali ndi Mtengo Wopatsa Moyo uja. (Gen 3:22-24)

10. Nanga Mulungu sadawadalitsenso?

Adawadalitsa, chifukwa adawalonjeza kuti adzawatumizira mpulumutsi yemwe adzawapulumutse ku tchimo lawo. (Gen 3:15)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe11:1-3*

Tikati kukhulupilira ndiye kuti kusakayika konse pa zinthu zimene tikuziyembekeza, ndiponso kutsimikiza kuti zinthu zimene sitikuziona zilipo ndithu. Pokhala ndi chikhulupiliro, makolo athu akale aja Mulungu adawaonetsa kuti ankakondwera nawo. Pokhala ndi chikhulupiriro timamvetsa kuti zonse zimene ziripo zidalengedwa ndi mawu a Mulungu, mwakuti zinthu zoonekazi zidachokera ku zinthu zosaoneka.

[1] Calvin " (Mulungu) ndikumuchotsera chinthu chofunikira kwambiri, tikamukaniza chizindikiro ichi.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO: 3
KUKULA KWAKE KWA TCHIMO

1. Kodi tchimo lidawonekera bwanji mmbanja la Adamu ndi Eva?

Kaini adadana ndi kupha mbale wake Abele, yemwe anali mwana wokhulupilira Mulungu. (Gen 4:8)

2. Kodi Mulungu adampatsa ndani mmalo mwa Abele?

Mulungu adampatsa Seti, munthu woopa Mulungu, yemwe ana ake anatchulidwa "ana owopa Mulungu." (Gen 4:25; 5:6-7; 6:2)

3. Kodi uchimo udapitilirabe mdziko lapansi?

Inde, ana a Kaini anapitilira kukhala oyipa, ndipo mitima ya anthu a paaaa dziko lonse lapadziko lonse linachimwirachimwira. (Gen 6:5)

4. Ndi chiyani chinapangitsa kuti uchimo ukulirekulire?

Ana a Kaini anali omveka ndi otchuka pa dziko lonse komanso anali oipa kwambiri. (Gen 6:4)

5. Kodi mungatchulepo ena mwa anthu otchukawa?

Inde, Baibulo limatiuza za Lameki wopha anthu ndi ana ake atatu: Yabala, Yubale ndi Tubala-Kaini. (Gen 4:18-24)

6. Kodi palinso china chimene chinapangitsa kuti tchimo likulirekulire?

Inde, chigumula chisanafike, anthu ankakhala moyo zaka zopitilira 900. (Mwachitsanzo Gen 5:5, 11, 14, 20)

7. Kodi ana onse a Seti anali oopa Mulungu?

Ambiri anakwatira ana a Kaini pomwe ochepa okha ndiwo ankatumikira Mulungu. (Gen 6:1-3)

8. Tchulani ena mwa ochepawa amene ankaopa Mulungu.

Enoki, amene anayenda ndi Mulungu, ndipo analosa za kubwera kwa Ambuye kudzaweruza dziko la pansi. (Gen 5:22-24; onaninso Yuda 14-15)

9. Ndi chiyani chinachitika kwa Enoki?

Mulungu anamutenga kupita naye kumwamba ali ndi zaka 365 zokha. (Gen 5:23-24, onaninso Ahe 11:5)

10. Kodi Mulungu anakelera kuti uchimo upitilire?

Ayi, pamene nthawi inakwana kuti aweruze dziko lapansi nthawi ya Nowa, Mulungu analengeza za chigumula. (Gen 6:3, 5-8, 11-14, 17)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:4, 5.*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Abele adapereka kwa Mulungu nsembe yopambana ya Kaini, navomerezedwa kuti ndiwolungama, chifukwa Mulungu mwiniwake adamchitira umboni pakulandira zopereka zake. Mwakuti ngakhale iye adafa, koma chifukwa cha chikhulupiliro chakecho, akulankhulabe mpaka pano. Pokhala ndi chikhulupiliro, Enoki adatengedwa kupita kumwamba, osafa konse. Sadapezekenso, popeza kuti Mulngu adamtenga. Malembo amamchitira umboni kuti asanatengedwe anali wokondweretsa Mulungu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
CHIGUMULA

1. Kodi Mulungu adalanga bwanji dziko loyamba lija?

Mulungu adalanga dziko lonse lochimwa lija ndi chigumula choopsa. (Gen 7:4, 10, 12)

2. Chigumulacho chinali chokula bwanji?

Chigumulacho chinakwanira dziko lonse lapansi ndipo chilichonse chamoyo chinaonongedwa. (Gen 7:18-23)

3. Kodi chigumula chimenechi chinabwera ndi mvula wamba?

Ayi, zinali zodabwitsa zedi, chifukwa kuthambo kudatseguka ndipo akasupe onse okhala pansi pa dziko adatumphuka. (Gen 7:11)

4. Ndi liti limene Mulungu adalengeza za chigumulachi?

Zaka 120 chigumula chisanafike, nthawi yomwe Nowa adapanga chombo ndikulalika za chilungamo. (Gen 6:3; onaninso Ahe 11:6-7; 2 Pet 2:5)

5. Mulungu adapulumutsa yani mchombo muja?

Nowa ndi a mbanja mwake ndi nyama zochepa za mtundu ulionse wopezeka pa dziko. (Gen 7:1-3, 7-9, 13-16)

6. Chifukwa chiyani Mulungu adapulumutsa Nowa ndi banja lake?

Chifukwa cha chisomo cha Mulungu, Nowa anali munthu wa chilungamo mdziko la anthu ochimwa. (Gen 6:8; 7:1; onaninso Ahe 11:6-7; 2 Pet 2:5)

7. Kodi chigumula chidatenga nthawi yotalika bwanji?

Madzi aja adakhalapobe mpaka masiku 150, ndipo Nowa adakhala mchombo muja chaka ndi masiku khumi. (Gen 7:24; 8:1-19)

8. Mulungu adamuuza chiyani Nowa chitangotha chigumula?

"Tsopano ndikuchita nawe chipangano pamodzi ndi zidzukulu zako ndi za moyo zonse zomwe zidatuluka nawe mchombo." (Gen 9:9-10)

9. Kodi Mulungu adapereka chizindikiro chotani cha chipangano chake ndi Nowa?

Chizindikiro cha utawaleza wa mmitambo. (Gen 9: 8-17)

10. Chigumula chidachitika liti?

Zaka 2350 Ambuye Yesu asanabadwe [2]

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:6-7.*

Ndipotu popanda chikhulupiliro nkosatheka kukondweretsa Mulungu. Paja aliyense wofuna kuyandikira kwa Mulungu, ayenera kukhulupilira kuti Mulunguyo alipodi, ndipo kuti amawapatsa mphotho anthu omufunafuna. Pokhala ndi chikhulupiliro, Nowa adalandira machenjezo a Mulungu onena za zinthu zomwe mpaka nthawi imeneyo zinali zisanaoneke. Adamvera napanga chombo kuti apulumutse onse a mbanja mwake. Potero, adawatsutsa kuti ngolakwa anthu a d[2]ziko lapansi, nalandira chilungamo chimene Mulungu amapatsa anthu omkhulupilira.

[2] James Ussher, Mbiri ya Chipangano Chakale, yotengedwa kuchokera mu buku lotchedwa "zoyombirira za Dziko Lapansi"

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 5
KUCHOKA KWA NOWA KUFIKA KWA ABRAHAMU

1.Kodi tchimo linatha ndi chigumula?

Ayi ndithu, linaonekera mbanja la Nowa chitangopita chigumula.(Gen 9:21-22.)

2. Kodi izi zinachitika bwanji?

Nowa ataledzera vinyo, Hamu adamuseka. (Gen 9:22)

3. Pambuyo pake, Nowa adachita chiyani?

Anamdalitsa Semu ndi Yafeti, koma anatemberera Kanani mwana wa Hamu. (Gen 9:24-27)

4. Kodi palinso njira ina yomwe tchimo linawonekera?

Inde, chifukwa anthu oipa anakakhala ku Sinala ndi kumanga nsanja ya Babele ndi mzinda wotchuka. (Gen 11:2-4)

5. Chidalakwika ndi chiyani ndi kumanga nsanja?

Zidasonyeza kunyada kofuna kufanana ndi Mulungu pomanga nsanja yofika kumwamba.

6. Chidakwika nchiyani pamene anthu anafuna kumanga mzinda waukulu?

Mulungu adauza anthu kuti amwazikane pa dziko lonse osati akhale pamodzi ndi kukhala otchuka. (Gen 11:4; onaninso 9:1)

7. Kodi Mulungu adalepheretsa bwanji maganizo awo?

Adasokoneza chilankhulo chawo kotero kuti adamwazikana pa dziko lonse. (Gen 11:5-9)

8. Kodi ana a Nowa adakakhala kuti?

Ana a Hamu anakakhala ku Kanani ndi ku Afirika, a Semu anakakhala ku Asia ndipo a Yafeti anakakhala ku Ulaya (Europe).[3]

9. Kodi Mulungu anapitiliza chipangano chake ndi ana a ndani chitatha chigumula?

Mu nthawi ya Chipangano cha Kale, Mulungu adapitiliza Chipangano chake ndi ana a m'banja la Semu. (1 Mbi 1:24-27)

10. Mwa ana a m'banja la Semu, Mulungu adachita Chipangano ndi ndani?

Abrahamu ndi ana ake. (1 Mbi 1:24-27; onaninso Gen 17:1-9)

*Ntchito ya pa mtima**:** Ahe 11:8*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Abrahamu adamvera pamene Mulungu adamuitana kuti apite ku dziko lina limene adamulonjeza kuti lidzakhala lake. Ngakhale sankadziwa kumene ankapita, iye adapitabe.

[3] Onani Ndemanga za Henry Pa 1 Mbiri 1: 1-27

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
ABRAHAMU

1. Kodi Mulungu adamuitana Abrahamu kuchokera m'dziko liti?

Mulungu adamchotsa mdziko la Uri wa ku Kaldeya, ndipo kenako adamuitana kuti achoke mdziko la Harani.(Gen 11:29-31; 12:1-4)

2. Kodi Mulungu adamuuza Abrahamu kuti chiyani?

"Choka ku dziko kwako kuno ...ndipo upite ku dziko limene nditi ndikusonyeze." (Gen 12:1)

3. Kodi Abrahamu adamvera?

Inde, ndi chikhulupiliro Abahamu adamvera, ndipo adapita kukakhala mlendo mdziko la Kanani. (Gen 12:4-5; Machit: 7:2-6; Ahe:11: 8)

4. Ndi liti limene Mulungu adamuitana Abrahamu?

Mchaka cha 2090 Ambuye Yesu asanabadwe

5. Kodi Abrahamu adapita ndi yani?

Loti mphwake, amene adasiyana naye ndi kukakhala ku Sodomu. (Gen 13:1, 7-12)

6. Abrahamu adakomana ndi ndani atampulutsa Loti kwa mfumu ya ku Elamu?

Melekizedeki, mfumu ya ku Salemu komanso wansembe wa Mulungu wopambambana zonse. (Gen 14:9-18)

7. Kodi chinachitika nchiyani ku mizinda yoipa ya Sodomu ndi Gomora?

Mulungu adawononga mizinda imeneyi ndi moto atapulumutsa Loti ndi banja lake. (Gen 19:22-25, 29)

8. Kodi Mulungu adamulonjeza chiyani Abrahamu?

Adamulonjeza kuti adzamusandutsa kholo la mtundu waukulu, dziko la Kanani lidzakhala la zidzukulu zake ndipo adzakhala chizindikiro cha madalitso mwa Khristu. (Gen 12:2-3; 15:13-16; 17:7-8; 18:17-18, onaninso Ahe 11:8-10, 13-16)

9. Kodi pa nthawiyi Abrahamu anali ndi ana?

Ayi, koma anakhulupilira lonjezo la Mulungu. (Gen 16:1; onaninso Ahe 11:8-12)

10. Kodi Mulungu adalonjeza chiyani kwa Abrahamu ndi Sara mu ukalamba wawo?

Adawalonjeza mwana, Isaki, ndipo kudzera mwa iye Mulungu adzakhazikitsa chipangano chake. (Gen 17:15-21; 18:10-15)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:9-10*

Pokhala ndi chikhulupirilo chomwecho, Abrahamu ankakhala ngati mlendo mdziko limene Mulungu adamulonjeza. Ankakhala mmahema pamodzi ndi Isaki ndi Yakobe, amene nawonso anali atalandira lonjezo lomwelo la Mulungu. Monsemo Abrahamu ankadikira mzinda wa maziko okhazikika. Mzindawo, Mmisiri woganiziratu mamangidwe ake ndiponso woumanga ndi Mulungu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
ISAKI

1. Kodi ana awiri a Abrahamu anali ndani?

Isimaele, mwana wa Hagara, ndi Isaki mwana wa Sara. (Gen 16:15; 21:2-3)

2. Kodi Mulungu adakhazikitsanso Chipangano chake ndi Isimaele?

Ayi, koma ndi Isaki yekha, mwana wolonjezedwa kwa Abrahamu uja. (Gen 17:16, 19-21)

3. Chidachitika ndi chiyani kwa Isimaele?

Pamene adamuyoza Isaki, Mulungu adamulamula Abrahamu kuti amchotse pamodzi ndi mayi wake. (Gen 21:8-12)

4. Kodi Mulungu adayesa bwanji chikhulupiliro cha Abrahamu pamene Isaki anali wamn'gono.

Mulungu adamulamula Abrahamu kuti akampereke mwana wake nsembe ku phiri la Moriya. (Gen 22:2-4)

5. Kodi Abrahamu adamvera?

Inde, chifukwa adakhulupilira kuti Mulungu atha kuukitsa Isaki kwa akufa. (Ahe 11:17-19)

6. Isaki adakwatira ndani?

Rebeka, mkazi woopa Mulungu, amene mtumiki wa Abrahamu anakamtenga ku Harani. (Gen 24:2-4, 50-51, 63-67)

7. Chifukwa chiyani Abrahamu adatuma wantchito wake ku Harani kukamutengera mwana wake Isaki mkazi?

Sadafune kuti akwatire mkazi wa Chikanani. (Gen 24:3)

8. Kodi Isaki ndi Rebeka adabereka ana?

Poyamba sanabereke ana, koma Mulungu atamva pemphero lawo adabereka ana amapasa, Esau ndi Yakobo. (Gen 25:21-26)

9. Mwa ana awiriwa, wodzasunga lonjezo la Mulungu anali ndani?

Mwana wamn'gono uja, Yakobo, yemwe Mulungu ankankonda kwambiri. (Gen 25:23; onaninso Machit 7:32; Aroma 9:13)

10. Esau anaonetsa bwanji kuti anali oyipa?

Anagulitsa ukulu wake, anakwatira akazi a Chikanani ndipo anafuna kupha Yakobo. (Gen 25:29-34; 26:34; 27:41-42)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:11-12*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Sara yemwe adalandira mphamvu zakutenga pathupi, ngakhale zaka zake zakubala mwana zinali zitapita kale. Zimenezi zidatheka chifukwa adavomera kuti amene adazilonjezayo ngokhulupilika. Nchifukwa chake mwa munthu mmodzi, wotinso anali ngati wakufa, mudatuluka mibadwo yochuluka ngati nyenyezi, ndi yosawerengeka ngati mchenga wa pa gombe la nyanja.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
YAKOBO

1. Yakobo adachita chiyani pamene Isaki anali pafupi kumpatsa madalitso?

Ndi malangizo oyipa amai ake, Yakobo adalandira madalitso atanamiza bambo wake omwe anali osaona. (Gen 27:6-27)

2. Kodi Esau adamudalitsanso?

Ayi, popeza chipangano cha madalitso chinali cha Yakobo yekhayo basi. (Gen 27:32-37, Ahe 12:16-17)

3. Essau adakonza zotani atazindikira kuti Isaki anadalitsa Yakobo.

Adakonza zopha Yakobo ndipo Yakobeo adathawira kwa malume wake Labani mdziko la Harani. (Gen 27:41-43)

4. Chidachitika ndi chiyani ku Betele pamene Yakobo ankathawa kupita kwa malume ake Labani?

Mulungu adamuonekera mmaloto ndi kumulonjeza madalitso omwe adapereka kwa Abrahamu ndi Isaki. (Gen 28:11-19)

5. Yakobo adakhala zaka zingati kwa Labani?

Zaka 20, ndipo ali komweko anakwatira Leya ndi Rakele ndipo analemera kwambiri. (Gen 29:16-28; 31:36-41)

6. Kunachitika chiyani pamene Yakobo ankabwerera ku Kanani?

Adalimbana ndi mngelo wa Mulungu pa malo otchedwa Penuele. (Gen 32:24-26)

7. Yakobo adaphunzirapo chiyani pa zomwe zinachitika ku Penuele?

Adaphunzira kuyembekezera madalitso ochokera kwa Mulungu, komanso adapatsidwa dzina latsopano, Isalaeli. (Gen 32:27-30)

8. Mulungu adampatsa Yakobo ana angati?

Mkazi mmodzi ndi amuna 12, omwe anakhala makolo a fuko la Isalaeli. (Gen 30:21; 35:22-26)

9. Kodi m'banja mwa Yakobo munali mtendere?

Ayi, munali nsanje ndi kukangana pakati pa akazi ndi ana ake. (Gen 37:1-11)

10. Abale a Yosefe anaonetsa bwanji kudana naye yosefe mwana wokondeka wa Yakobo?

Adamugulitsa kwa a Eguputo ngati kapolo, ndi kunamiza bambo awo kuti anagwidwa ndi chirombo cholusa. (Gen 37:20-32)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:13-14*

Onsewa adasunga chikhulupiliro chawo mpaka kufa. Sadalandire zimene Mulungu adawalonjeza, koma adangozionera chapatali ndi kuzikondwerera. Adavomera kuti pansi pano adalidi alendo osakhazikika. Paja anthu olankhula motere amaonekeratu kuti akufunafuna malo awo enieni okhazikikamo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
AISALAELI KU UKAPOLO

1. Kodi Mulungu adamusamala Yosefe ku Eguputo?

Inde, poyamba m'nyumba mwa Potifala, ku ndende, komanso ngati nduna yaikulu ya dziko la Eguputo (Gen 39:1-6, 20-23, 41:39-46)

2. Kodi Yosefe adaonana naonso abale ake?

Inde, nthawi yomwe abale ake anapita ku Eguputo kukagula chakudya nthawi ya zaka 7 za njala.(Gen 42:1-8)

3. Farao anachita chiyani atamva za bambo ndi abale ake a Yosefe?

Anatumiza ngolo kukawatenga kuti akakhale ku Eguputo, adawapatsa dziko la Gosheni kuti akhaleko.(Gen 45:9-10, 16-28; 46:26-30; 47: 1-6)

4. Yakobo asanamwalire adachita chiyani?

Anadalitsa ana ake onse komanso ana awiri a Yosefe.(Gen 48:8 – 49:28)

5. Kodi Yakobo ndi Yosefe analosera zotani za Isalaeli?

Kuti Mulungu adzawaombola ndi kuchoka ku Eguputo ndi kupita Kanani. (Gen 48:21; 50:24-25)

6. Ndi buku liti mBuku Loyera lomwe limafotokoza za ukapolo wa a Isalaeli ndi kuwomboledwa kwawo?

Buku la Eksodo, mawu omwe atanthauza 'kutuluka'.

7. Yosefe atamwalira a Isalaeli anaona zotani?

Farao watsopano anafuna kuwaononga. (Eks 1:6-10)

8. Iye ananzunza bwanji ana a Isalaeli?

Anawasandutsa akapolo, ndikulamula kuti ana onse aamuna aphedwe. (Eks 1:11-16)

9. Ataona mavuto osiyanasiyana, a Isalaeli anachita chiyani?

Analira kwa Mulungu kuti awapulumutse. (Eks 2:23-25)

10. Kodi Mulungu anasamala bwanji a Isalaeli kuukapolo?

Pamene anali kunzunzidwa, iwo anali kuchulukirachulukira. (Eks 1:12)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:15-16*

Akadakhala kuti ankaganizirako za kudziko kumene adaachokera, bwenzi atapeza danga lakuti abwerere kwakaleko. Koma monga momwe zilirimu tikuona kuti ankafuna dziko lina, lokoma kopambana, ndiye kuti dziko la Kumwamba. Nchifukwa chake Mulungu sachita manyazi kutchedwa Mulungu wao,popeza kuti adawakonzera mzinda.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
MOSE AWOMBOLA AISALAELI

1. Kodi Mulungu adawataya a Isalaeli panthawi ya ukapolo ku Eguputo?

Ayi, anawatumizira mtumiki wake Mose kuti akawaombole. (Eks 3:4 – 4:9)

2. Ndi liti Mose adayamba kugwira ntchito yake?

Pamene Mulungu adamuitana kuchokera pachisamba choyaka moto, m'dziko la Midiani. (Eks 3:1-3)

3. Kodi Mulungu adampatsa Mose ndani womuthandizira?

Aroni mbale wake kuti akhale mneneri. (Eks 4:10-17)

4. Kodi Farao anawalora a Isalaeli kuti apite pamene Mose adamuuza?

Ayi, Mulungu adaumitsa mtima wa Farao ndipo sadamvere malamulo ake. (Eks 4: 21; 5:1-2)

5. Ndi liti pamene Farao adawalora a Isalaei kuti apite?

Pamene Mulungu adawonetsa mphamvu zake powatumizira zozizwitsa zoopsa zokwana khumi. (Eks 9: 31-34)

6. Chozizwitsa chomaliza chinali chotani?

Ana onse achisamba a Eguputo anaphedwa, pamene ana a Isalaeli anapulumuka. (Eks 12:12-13, 22-23, 29)

7. Kodi pambuyo pake Aisalaeli anakumbukira bwanji kuomboledwa kwawo?

Ankachita phwando la Pasaka chaka chili chonse. (Eks 12:1-17; 24, 27)

8. Kodi Mulungu adadzeretsa a Isalaeli njira chidule popita ku Kanani?

Ayi, adadutsa ku chipululu podzera ku Nyanja Yofiira. (Exs 14:13-21)

9. Pa Nyanja Yofiira padachitika chiyani?

Mulungu adapanga njira youma pakati pa nyanjapo kuti Aisalaeli awolokerepo, koma ankhondo a Farao adamira pamene adafuna kuti awoloke. (Eks 14:22-30)

10. Kodi Aisalaeli adakhala ku Eguputo zaka zingati?

Pafupifupi zaka 400. (Eks 12:40-41; onaninso Machitidwe 7:6)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:17-19*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Abrahamu, pamene Mulungu adamuyesa, adapereka Isaki ngati nsembe. Ngakhale adali munthu woti Mulungu adampatsa lonjezo, adakhala wokonzeka kupereka nsembe mwana wake mmodzi yekhayo. Za mwana ameneyo Mulungu anali atanena kuti, "Mwa Isaki udzakhala ndi zidzukulu." Abrahamu ankakhulupilira kuti Mulungu atha kuukitsa munthu kwa akufa. Tsono tingathe kunena mofanizira kuti adamlandiranso Isakiyo ngati wouka kwa akufa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 11
ZAKA 40 MCHIPULULU

1. Kodi Mulungu adawatsogolera bwanji Aisalaeli mchipululu?

Ankawatsogolera ndi chipilala cha moto nthawi yausiku ndi chipilala cha mtambo nthawi ya masana. (Eks 13:21-22)

2. Mulungu adawadyetsanji Aisalaeli?

Mana wochokera kumwamba, ndi madzi wochokera muthanthwe.(Eks 16:13-15; 17:2-6)

3. Kodi Aisalaeli adakwanitsidwa nazo zomwe adalandira mchipululu?

Ayi, nthawi zambiri ankangodandaula ndi kumuukira Mose komanso Mulungu. (Eks 16:1-3; Num 20-1-5, 21:5)

4. Kodi poyamba Mululungu adakawakhazika kuti?

Ku phiri la Sinai komwenso Mulumgu adawapatsa malamulo khumi, mmene adzamangire guwa ndi malamulo ena ambiri. (Eks 19:20; 20:1-17; 25 – 28:43; 21 – 23:33)

5. Aisalaeli adachimwanji pamene Mose anali ku Phiri la Sinai?

Aisalaeli anapanga mwanawan'gombe wa golide ndi kumampembedza. (Eks 32:19-25)

6. Mulungu adawasiya Aisalaeli kuti atawachotsa ku Sinai?

Ku Kadesi, komwe anatuma amuna 12 kukazonda dziko la Kanani. (Num 13:1-30)

7. Anthu okazonda aja anasimba zotani?

Anasimba zoipa za dziko adakalizondalo, kupatula Yoswa ndi Kalebu, amene anakhulupilira kuti Mulungu adzawapatsa dzikolo.(Num 13:30-33, 14:6-9)

8. Anthuwo adamvera zomwe adasimba ndani?

Adamvera zoipa zomwe adasimba anthu khumi aja kuti dziko la Kanani linali lamphamvu kwambiri mwakuti sakadatha kuligonjetsa. (Eks 14: 1-4, 10)

9. Mulungu adawalanga bwanji chifukwa cha kupenekera kumeneku?

Ankangoyendeyenda mchipululu kwa zaka 40 kufikira onse azaka 20 ndi kupitilira apo atafa kungopatulapo Yoswa ndi Kalebu. (Eks 14:19-39)

10. Mulungu adapulumutsa bwanji Aisalaeli ku njoka zaululu zomwe adawatumizira kamba kakuwiringula kwawo?

Adauza Mose kuti apange njoka ya mkuwa ndipo aliyense wolumidwa akayan'gana njoka ya mkuwayo ankachira. (Eks 21:4-9)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:20-21*
Pokhala ndi chikhulupiliro adapemphera ana ake , Yakobe ndi Esau, madalitso a mtsogolo. Pokhala ndi chikhulupiliro, Yakobe pakufa, adadalitsa ana a Yosefe mmodzimmodzi. Pochita zimenezi anali atayedzamira pa ndodo yake akupwmbwdza Mulungu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
AISALAELI ALOWA MDZIKO LA KANANI

1. Ndani adatsogolera Aisalaeli pokalowa mdziko la Kanani?

Yoswa, mwana wa Nuni amene Mulungu adamusankha kulowa mmalo mwa Mose. (Yos 1:1-2)

2. Ndi dera liti la Kanani lomwe adalanda poyambilira?

Dera la kummawa kwa mtsinje wa Yorodani, mbali yomwe idaperekedwa kwa Rubeni,Gadi, ndi gulu lina la mtundu wa Manase. (Yos 12:1-6; onaninso Numeri 32)

3. Aisalaeli adawoloka bwanji mtsinje wa Yorodani?

Adawolokera pa malo ouma omwe Mulungu adawapangira pamtsinjewo. (Yos 3:5-17)

4. Aisalaeli adakwanitsa bwanji kulanda dziko la Kanani?

Mulungu adawamenyera nkhondo ndi kugonjetsa adani awo. (Yos 10:25)

5. Kodi zinali zodziwika ndithu kuti Mulungu adawamenyera nkhondo Aisalaeli?

Inde, zinadziwika ndithu kwa Aisalaeli ndipo izi zinadzetsa mantha kwa adani awo. (monga Yos 10:28-43)

6. Tchulani zinthu ziwiri zosonyeza kuti Mulungu ndiye anawalora kuti apambane.

Zipupa za mzinda wa yeriko zinagwa, komanso dzuwa linayima osayenda konse**.** (Yos 6:1-21, 10:12-14)

7. Kodi Aisalaeli adamvera Mulungu zoti aononge mtundu wonse wa a Kanani?

Ayi, adasiyako ena; ndipo iwowa ndi amene anabweretsa mavuto ku mtundu wa Aisalaeli pambuyo pake. (Yos 9:24; 17:12-13; Num 33:51-56; Owe 3:1; 4:1-3)

8. Kodi dzikolo lidagawidwa bwanji?

Fuko lililonse kupatula fuko la Levi lidalandira gawo la dzikolo pochita maere. (Yos 13:6, 14)

9. Yoswa asanamwalire anawachenjeza anthu ake zotani?

Za tchimo loopsa lopembedza milungu ya chilendo. (Yos 24:14-29)

10. Ndi liti pomwe Aisalaeli adalowa mdziko la Kanani?

Zaka 1405 Amuye Yesu asanabadwe.

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:22-23*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Yosefe ali pafupi kutsirizika, adanenapo za kutuluka kwa Aisalaeli ku Ejipito, nawauziratu za mmene adaayenera kudzachitira ndi mafupa ake. Pokhala ndi chikhulupiliro, atabadwa Mose, makolo a Mose adamubisa miyezi itatu, poona kuti mwana waoyo anali wokongola. Sadaope konse lamulo la mphamvu la mfumu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
OWERUZA

1. Kodi Aisalaeli anakumbukira chenjezo la Yoswa loti asadzapembedze mafano?

Pamene Yoswa anali ndi moyo anatsatiradi koma atamwalira anaiwala Mulungu wawo ndi kupembedza mafano. (Owe 2:8-13)

2. Kupembedza mafanoku kudadza bwanji?

Mitundu yonse ya chikanani yosakhulupira Mulungu ndi mafano awo sanaziwononge.(Owe 2:1-2)

3. Mulungu adawalanga bwanji Aisalaeli ndi kusamvera kwawoku?

anawapereka mmanja mwa adani awo ndikuwazunza. (Owe 2:3,14)

4. Mavuto awo ankatha nthawi yotalika bwanji akachimwa?

Pamene analapa ndi kubwerera kwa Mulungu. (mwachitsanzo Owe 3:9)

5. Mulungu adapulumutsa bwanji anthu ake?

Mulungu anawatumizira 'oweruza' kudzawapulumutsa. (Owe 2:16-18)

6. Nthawi ya oweruzayi inatha liti?

Zaka 400 kuyambira nthawi ya Yoswa kufikira nthawi ya Saulo. (Mach. 13:20)

7. Baibulo limakamba za oweruza angati?

14, ndipo maina awo ndi awa:

Otaniele	Tola	Abudoni
Ehudi	Jeya	Samusoni
Samaga	Yepita	Eli
Baraki (ndi Debora)	Ibzani	Samuele
Gidioni	Eloni	

8. Tchulani kholo lochuka la Ambuye Yesu Khristu amene anakhala nthawi ya oweruza.

Rute wa ku Mowabu, mmodzi wa mayi ake a Khristu. (Rut 1:1-5; onaninso Mat 1:5)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:24-26*

Pokhala ndi chikhulupiliro, Mose atakula adakana mdzukulu wa Farao, mfumu ya ku Egupto. Iye adasankha kunzunzikira nawo limodzi ana a Mulungu, koposa kukondwerera zosangalatsa za uchimo kanthawi pan'gono. Adaona kuti kunzunzika chifukwa cha Wodzozedwa wa Mulungu chinali chuma chachikulu koposa chuma chonse cha ku Eguputo pakuti maso ake anali ndithu pa mphotho ya kutsogolo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
OWERUZA (KUPITILIZA)

1. Gidioni atakhala oweruza adachita chiyani?

Adagonjetsa a Midiani ndi amuna 300 okha. (Owe 7:7-9, 12, 16-25)

2. Yefita adadziwika kwambiri chifukwa chiyani?

Ndi chikhulupiliro, Yefita adagonjetsa a Amoni. (Owe 11:30-33)

3. Ndi oweruza uti amene anathira nkhondo a Filisiti yekha?

Samusoni, wa ku Nazareti, ngakhale kuti sanali wokhulupirika kwenikweni. (Owe 13:1-5; 14:1-4; 16:30)

4. Tchulani zinthu zingapo zodziwika bwino zomwe Samusoni adachita.

Adazula ndi kutenga zitseko za pachipata cha mzinda wa Gaza, adapha a Filisiti 1000 ndi chibwano cha bulu, ndipo panthawi ya kufa kwake adagwetsa kachisi ndi kupha a Filisiti zikwizikwi. (Owe 15:13-20; 16:1-3, 23-30)

5. Ndi chiyani chomwe chikusonyeza kuti a Isalaeli adalekana ndi Mulungu pa nthawi imeneyi?

Nkhani yomvetsa chisoni ya Mika ndi wansembe wonama yemwe anthu a fuko la Dani adamubera. (Owe 17:5 – 18:31)

6. Kodi muweruzi wotsiriza anali ndani?

Samueli kutanthauza kuti "Ndidachita kupempha kwa Chauta" komanso anali mneneri. (1 Sam 1:20; 3:20)

7. Mulungu adapulumutsa bwanji a Isalaeli munthawi ya Samuele pamene iwo adatembenuka mtima?

Mvula ya mabingu, kotero kuti a Filisiti adathawa pamaso pawo. (1 Sam 7:9-13)

8. Ndi choipa chanji chomwe a Isalaeli adapempha Samuele atakalamba?

Adafuna kuti alingane ndi mafuko ena pokhala ndi mfumu yawoyawo. (1 Sam 8:4-21)

9. Mulungu adamuuza chiyani Samuele pa pempho lawo lofuna mfumu?

Adati a Isalaeli akana Chauta osati Samuele. (1 Sam 8:7)

10. Kodi Mulungu adawapatsa a Isalaeli mfumu?

Inde, Chauta adamuuza Samueli kuti adzawapatsa mfumu ankaifunayo. (1 Sam 8:22 – 9:2, 27 – 10:1)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:27-29*

Pokhala ndi chikhukhulupiliro, Mose adachoka ku Eguputo, osaopa ukali wa mfumu, popeza kuti ankapirira ngati munthu woona Mulungu osaonekayu. Pokhala ndi chikhulupiliro adachita nawo chikondwerero cha Pasaka, nalamula kuti anthu awaze magazi pa zitseko kuti mgelo woononga ana achisamba asakhudze ana achisamba a aIsalaele. Pokhala ndi chikhulupiriro , aIsalaeli adawoloka Nyanja Yofiira ngati pamtunda pouma. Koma a Ejipito, kuti nawo ayesere kuwoloka, adamizidwa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
MFUMU SAULO

1. Mfumu yoyambirira imene Mulungu anapereka kwa Isalaeli ndi ndani?

Saulo, mwana wa Kisi; wa fuko la Benjamini. (1 Sam 9: 1-2, 27 – 10:1)

2. Saulo asankhidwa liti kukhala mfumu?

Mzaka za 1043 Ambuye Yesu asanabadwe (BC).

3. Kodi Saulo anali woopa Mulungu?

Ayi, anawonetseratu koyamba komwe kuti sankasamala malamulo a Mulungu. (mwachitsanzo 1 Sam 15:10-11)

4. Kodi Saulo anaonetsa bwanji kuti ndi wosamvera Mulungu asanachite nkhondo ndi Afilisti?

Popereka yekha nsembe mmalo momudikira Samuele kuti abwere. (1 Sam 13:7-14)

5. Kodi tchimo lachiwiri lalikulu lomwe Saulo anachimwa pamene ankamenyana ndi a Amaleki ndi lotani?

Sadamvere Mulungu pomusiya Mfumu Agagi wamoyo ndi ziweto zina zabwino (1 Sam 15: 2-11).

6. Samueli adamuuza Saulo chiyani atachimwa kachiwiri?

Mulungu adamukana Saulo kuti asakhalenso mfumu, ndipo kuti adzapereka ufumu wa Isalaeli kwa mzake. (1 Sam 15:16-30)

7. Ndani anasankhidwa kukhala mfumu mmalo mwa Saulo?

Davide, mwana mwa Jese, wa fuko la Yuda, munthu wa kumtima kwake kwa Mulungu.
(1 Sam 13:14; 16:11-13; onaninso Machitidwe 13:22)

8. Kodi Davide anakhala mfumu nthawi yomweyo?

Ayi, anadikira Saulo atamwalira kuti Mulungu ampatse ufumu. (2 Sam 2:1-5)

9. Kodi Saulo ankamkonda Davide?

Ayi, Davide sadamchitire Saulo choipa chirichonse, ngakhale Saulo adafuna kumupha kangapo konse. (Mwachitsanzo 1 Sam 20:30-33; 23:6-8; 24:1-6)

10. Saulo adamwalira bwanji?

Adatsiriza zaka 40 za ufumu wake podzipha yekha atagonja pa nkhondo ya Afilisti. (1 Sam 31:1-6)

*Vesi loloweza pamtima**:** Aheberi 11: 30-31*

Pokhala ndi chikhulupiliro, malinga a mzinda wa Yeriko adagwa, Aisalaeli atawazugulira masiku asanu ndi awiri. Pokhala ndi chikhulupiliro, Rahabu mkazi wa dama uja, sadafe nawo limodzi anthu osamvera aja, adaawalandira bwino azondi aja kunyumba kwake.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
MFUMU DAVIDE

1. Kodi Davide adalamulira kwa zaka zingati?

Zaka 7 ku Yuda kokha ndipo zaka 33 m'dziko lonse la Isalaeli. (2 Sam 5:4-5)

2. Mulungu adamudalitsa bwanji Davide ngati mfumu?

Chifukwa cha kupambana kwake, Mulungu adaapatsa a Isalaeli dziko lonse kuchokera ku mtsinje wa Yufureti mpaka ku Eguputo. (2 Sam 8:1-14; 1 Mbi 13:5-6)

3. Kodi Davide adabweretsanji ku Yerusalemu ali ndi chimwemwe chachikulu?

Likasa la Chipangano lomwe kuchokera nthawi ya Eli, linali mnyumba mwa Abinadabu. (2 Sam 6:1-17)

4. Kodi Davide anali wokhutitsidwa atabweretsa likasalo ku Yerusalemu?

Ayi, koma anafunanso kumanga nyumba ya Mulungu ku Yerusalemuko. (2 Sam 7:1-5; 1 Maf 8:17)

5. Kodi Mulungu adamuuzanji Davide za nkhaniyi?

Kudzera mwa mneneri Natani , Mulungu adamuuza Davide kuti mwana wake ndi amene adzamange nyumbayo. (2 Sam 7:11-17; 1 Maf 8:18-19)

6. Mulungu adamulonjeza Davide chiyani?

Adalonjeza kuti ufumu wa Davide udzakhazikika mpaka muyaya.(2 Sam 7:16)

7. Kodi lonjezoli limaloza kwa ndani?

Kwa Ambuye Yesu Khristu, omwe ufumu wawo ngosatha. (Mt 1:1; 22:41-46; Lk 1:31-33; Yes 9:6-7; 2 Pet 1:11; Chiv 11:15)

8. Kodi Davide adaloserapo za Khristu?

Inde, pafupifupi mMasalimo ake onse omwe adalemba.(mwachitsanzo Mas 2; 22; 45; 72; 110 ndi ena)

9. Kodi tchimo loopsa lomwe Davide adachita ndi lotani?

Adagona ndi Batesheba ndi kupha mwamuna wake Uriya. (2 Sam 11:2-17)

10. Ndi chiyani chinamubweretsera Davide mavuto ndi chisoni muulamuliro wake?

Kuukira ndi imfa ya mwana wake Abisalomu. (2 Sam 15:1-17; 18:9-17, 32-33)

Vesi loloweza pa mtima: Ahe 11:32-33

Kodi ndinenenso chiyani tsopano? Nthawi yachepa yoti ndinene za anthu enanso ambiri monga Gidiyoni, Samisoni, Yefita, Davide, Samuele ndiponso aneneri. Pokhala ndi chikhulupiliro anthu amenewa adagonjetsa maufumu, adakhazikitsa chilungamo, ndipo adalandira zimene Mulungu adaawalonjeza. Ena adapuya mikango pakamwa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 17
MFUMU SOLOMONI

1. Ndani adakhala mfumu Davide atamwalira?

Mwana wake Solomoni, amen analamulira mzaka za 971 Ambuye Yesu asanabadwe. (1 Maf 1: 32-35, 38-40; 2:1-4, 11-12)

2. Kodi Solomoni anali mfumu yoopa Mulungu?

Inde, adakonda Mulungu ndipo adasunga malamulo a bambo wake Davide. (mwachitsanzo 1 Maf 2:23-24; 3:3; 8:22-54)

3. Solomoni adapempha chiyani kwa Mulungu?

Mulungu atamuonekera mmaloto, Solomoni adapempha nzeru kuti athe kulamulira bwino anthu a Mulungu. (1 Maf 3:5-10)

4. Mulungu adampatsa chiyani Solomoni?

Adampatsa nzeru zambiri, komanso chuma ndi ulemu.(1 Maf 3:11-14; 4:29-31)

5. Ndani adadzamuyendera Solomoni?

Mfumukazi ya ku Sheba, yemwe anabwera kudzamva za nzeru zake, ndi kuona ulemelero wake. (1 Maf 10:1-9)

6. Zambiri zokhudza nzeru za Mfumu Solomoni tizipeza mmabuku ati a m'Baibulo?

Miyambo, Masalimo, Mulaliki ndi Nyimbo ya Solomoni.

7. Kodi Solomoni adamenya nkhondo zambiri ngati mmene Davide adachitira?

Ayi, chifukwa munthawi ya ulamuliro wake, kunali mtendere ndi chitukuko (1 Maf 4:21-25)

8. Kodi Solomoni adamanga Nyumba ya Chauta monga momwe Chautayo adamuuzira Davide?

Inde, Solomoni adamanga Nyumba ya Chauta yokongola ndi ya mtengo wapatali ku Yerusalemu. (1 Maf 6:1-10)

9. Chifukwa chiyani Solomoni adafulatira Mulungu?

Akazi ake achikunja amene adawamangira nyumba zopembezeramo mafano awo. (1 Maf 11:1-8)

10. Solomoni atachimwa choncho, Mulungu adamuuza kuti chiyani?

Adzalanda mafuko onse kupatula mafuko a Yuda ndi Benjamini kuchokera kwa Davide ndi kuwapereka kwa munthu wina (1 Mafumu 11: 9-13 onaninso 12:21, 23).

*Vesi loloweza pa mtima**:** Ahe 11:34-35*

Ena adazimitsa moto waukali, ndipo ena adapulumuka, osaphedwa ndi lupanga. Anali ofooka koma adalandira mphamvu. Adasanduka ngwazi pa nkhondo, nathamangitsa magulu a ankhondo a adani awo. Akazi ena adalandiranso anthu awo amene adafa, atawaukitsa. ena adanzunzidwa koopsa mpaka kufa, osalola kuti awamasule, chifukwa chofuna kudzazukanso ndi moyo wabwino kopambana.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
UFUMU UGAWANIKA

1. Solomoni atafa, ufumu udagawanika bwanji?

Mafuko ambiri adachoka mbanja la Davide ndi kutsatira Yerobowamu. (1 Maf 12:12-20)

2. Ndi mafuko ati amene adakhalabe okhulupirika kwa Rehobowamu, mwana wa Solomoni?

Yuda, ndi ena a fuko la Benjamini ndi Simioni, omwe anali a Ufumu wa Yuda. (1 Maf 12:21, 23)

3. Ufumu wa mafuko 10 aja unkatchedwa kuti chiyani?

Ufumu wa Israele, omwe likulu lake linali mzinda wa Samaria. (1 Maf 12:19-20; 16:20-29)

4. Kunali kulondola kuti mafuko 10 amenewa apatukane?

Ayi, linali tchimo lalikulu zedi chifukwa adasiya banja la chifumu la Davide lomwenso ndi nyumba ya Mulungu. (1 Maf 12:16, 19, 25-29)

5. Kodi Rehobowamu adafunitsitsa kuti mafuko 10 aja abwererenso?

Inde, adafuna kuchita nkhondo ndi Yerobowamu, koma Mulungu adamuletsa kutero. (1 Maf 12:21-24)

6. Chifukwa chiyani Mulungu adamuletsa Rehobowamu kuchita nkhondo?

Adafuna kulanga tchimo la Solomoni polekanitsa fuko la Israeli. (1 Maf 11:9-13; 12:24a)

7. Kodi Mulungu adatayiratu ufumu uja wa mafuko 10?

Ayi, ankawatumizira aneneri kukawachenjeza za machimo awo. (onani monga 1 Maf 13:1-3; 16:1-7)

8. Kodi anasiyana bwanji ndi Israeli?

Ufumu wa Yuda unali wosankhidwa ndi Mulungu ndipo Mulungu anasunga lonjezo lake ndi Davide ndi iwo. (onani mwachitsanzo 1 Maf 15:9-15; 2 Maf 8:16-19; 22)

9. Chinachitika nchiyani ndi ufumu wa Israeli?

Analekana ndi Mulungu ndipo patapita zaka 250 anatengedwa ku ukapolo ndi dziko la Asiriya ndiponso anabalalika ponseponse.(2 Maf 15:29; 17:5-6; 1 Mbi: 5:26; Machit 2:5-11)

10. Chinachitika nchiyani ndi ufumu wa Yuda?

Yuda nayenso analekana ndi Mulungu, ndipo patatha zaka 400 anatengedwa ku ukapolo ku Babeloni. (2 Maf 25:20-21)

*Vesi loweza pamtima**:** Ahe 11:36-37*

Ena, anthu adawaseka ndi kuwakwapula. Adamangidwa ndi maunyolo naponyedwa mndende. Ena adawapha pakuwaponya miyala; ena adawacheka ndipo ena adawapha ndi lupanga. Ankayenda uku ndi uku atavala zikopa za nkhosa kapena za mbuzi, umphawi wokhawokha, anthu nkumawazunza ndi kuwavutitsa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
ISRAELI -KUCHOKERA PA YEROBOWAMU KUFIKIRA AHABU

1. Ndi tchimo lanji lomwe a Israeli sadalisiye mmbiri yawo?

Tchimo lochokera kwa Yerobowamu mwana wa Nebati, yemwe anaphunzitsa a Israeli kupembedza Mulungu pogwiritsa ntchito mwana wa n'gombe wa golide. (1 Maf 12:26-30, 2 Maf 3:1-3; 10:28-31; ndi ena)

2. Ilipo mfumu ina ya a Israeli imene inatumikira Mulungu mokhulupirika?

Ayi, onse anali oipa, ena kuposa Yerobowamu. (mwachitsanzo 1 Maf 15:25-26, 33-34; 16:7, 25)

3. Kodi mafumu onse a aIsraeli ankachokera mbanja la Yerobowamu?

Ayi, kawirikawiri Mulungu ankalanda ufumu kwa mfumu ina ndi kuupereka kwa wina.

4. Baibulo likuti chiyani za Omuri mfumu nambala 6?

Anali oipitsitsa kuposa mafumu ena onse iye asanakhale mfumu. (1 Maf 16:25-26)

5. Ndani adakhala mfumu pambuyo pa Omuri?

Ahabu, mwana wake amene analinso woipitsitsa.(1 Maf 16:29-30)

6. Tchimo la Ahabu linali lotani?

Adakwatira mkazi wa chikunja, Yezebele ndi kuphunzitsa a Israeli kupembedza Baala. (1 Maf 16:31-33)

7. Ndi chiyaninso chimene Ahabu ndi Yezebele anachita?

Adaimba milandu ndi kupha aneneri a Mulungu. (1 Maf 18:3-4, 13)

8. Kodi Mulungu adadziwonetsa kudzera mwa mneneri uti kuti Iye ndiye Mulungu osati Bala?

Mneneri Eliya yemwe anamuuza Ahabu kuti sikudzagwanso mvula kufikira Eliyayo ataipempherera. (1 Maf 17:1)

9. Ndi liti pamene mvula inagwa?

Patapita zaka ziwiri ndi theka pamene aIsraele anaulula kuti Mulungu ndiye Ambuye. (Yakobo 5:17-18)

10. Kodi Mulungu anali ndi anthu ake ku Israeli m'nthawi ya Ahabu?

Inde, Mulungu anamuuza Eliya kuti panali anthu okwana 7 000 amene sanagwade kwa Baala. (1 Maf 19:18; Rom 11:4)

*Vesi loloweza pamtima**:** Ahe 11:38-40*

(Anthu amenewa, pansi pano sipadawayenere:) Ankangoyenda mzipululu ndi m'mapiri namabisala m'mapanga ndi m'mayenje a pansi. Anthu onsewa, ngakhale adawachitira umboni wokoma chifukwa cha chikhulupiliro chawo, sadalandire zimene Mulungu adaalonjeza. Ndiye kuti Mulungu anali ataganiziratu zotikonzera zabwino zopambana kotero kuti sadafune kuti anthu onse aja asafikire ku ungwiro popanda ife.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
AISRAELI- KUCHOKERA NTHAWI YA AHABU KUFIKA NTHAWI YA UKAPOLO

1. Kodi Mulungu adaononga banja la Ahabu kudzera mwa ndani?

Yehu, amene Mulungu anamusankha kuti agwire ntchitoyi. (2 Maf 9:30 – 10:11, 17)

2. Kodi Yehu anali woopa Mulungu?

Ayi, popeza anaononga banja la Ahabu chifukwa cha ubwino wa iye mwini. (2 Maf 10:27-31)

3. Umboni wa zimenezi ndi wotani?

Yehu sanasiye zoipa za Yerobowamu mwana wa Nebati. (2 Maf 10:29, 31)

4. Ndani analosera m'nthawi ya Yehu?

Elisa, yemwe anachita zozizwitsa zambiri. (mwachitsanzo 2 Maf 4:1-8, 31-37; 6:15-20)

5. M'dani wamkulu wa aIsraeli anali ndani nthawi imeneyi?

Ufumu wa a Siriya, omwe a Isaraeli adawagonjetsa kambirimbiri. (mwachitsanzo 2 Maf 6:15-20; 7:1-7)

6. Kodi banja la Yehu linalamulira Israeli nthawi yotalika bwanji?

Kufikira mbadwo wa chinayi, koma nthawi yonseyi palibe anasiya kupembedza ana a ng'ombe a golide. (2 Maf 15:12)

7. Kodi mafumu awiri a aIsraeli opambana zedi a mbanja la Yehu ndiwo ati?

Yehowasi ndi Yerobowamu Wachiwiri, amene adagonjetsa Asiriya kambirimbiri Asiriya. (2 Maf 13:24-25; 14:23-27)

8. Ndani adalosera pa nthawi ya mafumu omaliza a Israeli?

Hoseya, amene adachenjezeratu za chiweruzo cha a Isaraeli. (Hos 1:1 ndi mdime zotsatira)

9. Ndi ufumu uti wotchuka umene unatenga a Israeli ku ukapolo?

Asiriya omwe anakhala mdziko la aIsraeli ndi anthu ena a mdziko lina ndipo pambuyo pake ankatchedwa a Samariya (2 Maf 17:1-6, 24)

10. Aisraeli anapita kuukapolo chaka chanji?

Mchaka 722 Ambuye Yesu asanabadwe.

*Ntchito yoloweza pamtima**:***
Lowezani pamtima maina a mafumu a aIsraeli otsatirawa:

Yerobowamu	Tibini	Yehu	Salumu
Nadabu	Omuri	Yehowahazi	Menahemu
Baasa	Ahabu	Yehowasi	Pekahiya
Ela	Ahaziya	Yerobowamu II	Peka
zimuri	Yehoramu	Zakariya	Hoseya

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
YUDA-KUCHOKERA NTHAWI REHOBOWAMU KUFIKIRA NTHAWI YA AHAZI

1. Kodi mafumu a Yuda ankachokera mmabanja osiyana ngati mmene zinalili ndi Israeli?

Ayi, onse ankachokera ku banja la chifumu la Davide.

2. Chifukwa chiyani izi zinali choncho?

Sikuti mafumuwa anali owopa Mulungu ayi koma kuti Mulungu ankasunga lonjezo lake ndi Davide. (2 Sam 7:16; onaninso Yes 9:6-7; Luk 1:31-33)

3. Ndiye kuti mafumu onse a mbanja la Davide sanali owopa Mulungu?

Ayi, ndi mafumu ochepa okha amene anatumikira Mulungu mokhulupirika.

4. Tchimo lawo lalikulu linali lotani?

Iwowo ankapembedza mafano, kapenanso ankalola anthu awo kusiya Mulungu ndi kupembedza mafano. (Mwachitsanzo 1 Maf 14:21-24; 2 Maf 8: 26-27)

5. Ndi chiyani china adachimwa kuwonjezera popembedza mafano?

Sadakhulupilire Mulungu nthawi zonse koma anapempha maiko kuti awathandize kumenyana ndi adani awo. (mwachitsanzo 2 Maf 3:7; 8:28)

6. Tchulani mafumu ena amene sanatumikire Mulungu.

Yehoramu, Ahaziya, mfumukazi Ataliya ndi Ahazi oipitsitsayo. (2 Maf 8:18-19, 27; 11:1-3; 16:2-4)

7. Tchulani mafumu ena amene anali abwino.

Asa ndi Yehosafati amene adayesetsa kuthetsa kupembedza mafano. (1 Maf 15:9-15; 22:42, 46; 2 Mbi 17:7-9)

8. Chidawononga ufumu wa Yehosafati ndi chiyani?

Adachita mgwirizano ndi Ahabu oipa uja ndipo mwana wake Yehoramu adakwatira Ataliya mwana wamkazi wa Ahabu. (2 Mbi 18:1-3; 21:6)

9. Mfumukazi Ataliya adachimwanji?

Adafuna kupha onse a mbanja la Davide koma mkazi wa wansembe wina woopa Mulungu, Yehoiwada adapulumutsa moyo wa mwana wa Yowasi mwana wa Ahaziya.(2 Maf 11:1-3)

10. Mfumu yoipitsitsa kuposa onse anai ndani?

Ahazi amene ankapembedza mafano, anatseka Nyumba ya Mulungu, ndi kumanga maguwa opembedzera mafano mu mzinda wa Yerusalemu. (2 Maf 16:1-18)

*Ntchito yololoweza pamtima**:***

Lowezani pamtima maina a mafumu a Yuda kuyambira nthawi ya Rehobowamu mpaka nthawi ya Ahazi motere:

Rehobowamu	Yehoramu	Amaziya
Abiya	Ahaziya	Uziya
Asa	Mfumukazi Ataliya	Yotamu
Yehosafati	Yowasi	Ahazi

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO: 22
YUDA- KUCHOKERA NTHAWI YA HEZEKIYA KUFIKIRA NTHAWI YA KU UKAPOLO

1. Ndi mfumu iti yomwe idabweretsa kusintha ku Yuda?

Hezekiya amene anali owopa Mulungu. (2 Maf 18:1-7)

2. Iye adachita chiyani?

Adatsekulanso Nyumba ya Mulungu, adaphwanya mafano onse, ndi kuwononga malo onse apamwamba omwe anthu ankapembedzera Yehova; komanso adauza kuti apitirize kuchita chikondwerero cha Pasaka. (2 Mbi 29:2-11; 30:1-8; 2 Maf 18:4)

3. Mulungu adawombola bwanji aIsraeli mmanja mwa a Siriya?

Pamene a Siriya adazinga mzinda a Yerusalemu, Mulungu adatuma mngelo wake ndi kuononga ankhondo okwana 185 000. (Yes 37:33-37)

4. Ndani anali mneneri wa Yuda nthawi imene Hezekiya anali mfumu?

Yesaya, yemwe Mulungu adamtuma kudzachenjeza anthu oipa ndi kutonthoza mitima ya anthu ake. (Yes 1:1-2, 9, 16-27, 2:1-5; 3:1-8; 4)

5. Kodi Yesaya analosera zotani?

Adauza Hezekiya kuti Yuda adzatengedwa kupita ku ukapolo ku Babiloni. (Yes 39)

6. Ndani adalowa ufumu mmalo mwa Hezekiya?

Manase, amene anali oipa kwamiri koma analapa ali kuukapolo. (2 Maf 20:21 – 21:2)

7. Mfumu Yosiya adachita chiyani adakali wamn'gono?

Adafunafuna Mulungu, adachotsa ndi kutaya mafano onse, ndi kuphunzitsa fuko la Yuda malamulo a Mulungu. (2 Maf 23:1-3,4-6, 24; 2 Mbi 34:3-7)

8. Ndi mneneri uti amene anakhalapo nthawi ya Yosiya mpaka nthawi ya ukapolo?

Yeremiya, amene anachenjeza fuko la Yuda za machimo awo ndi kuwauza kuti alape machimo awo. (Yer 1:1-2; 3:23 – 4:6 ndi ena)

9. Kodi mafumu ndi anthu a fuko la Yuda adamvera Yeremiya?

Ayi, ndipo chifukwa cha machimo awo adatengedwa kupita ku ukapolo ku Babiloni. (Yer 25:1-10; 2 Mbi 36:1-7)

10. Ndi chaka chiti pomwe Nebukadineza adaononga mzinda wa Yerusalemu?

586 Ambuye Yesu asanabadwe

*Ntchito yololoweza pamtima**:***

Lowezani pa mtima maina a mafumu awa ku Yuda kuyambira nthawi ya Hezekiya mpaka nthawi ya Zedekiya:

Hezekiya	Yosiya	Yehowakimu
Manase	Yehowahazi	Yehowakini
Amoni		Zedekia

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 23
YUDA KUFIKIRA NTHAWI YA UKAPOLO

1. Kodi Yuda adakhala nthawi yaitali bwanji ali kuukapolo?

Zaka 70, monga momwe Yeremiya adalosera.(Yer 25:11-12)

2. Kodi aYudawa analapa ku ukapoloko?

Inde, ochepa okha adalapa ndi kulilira mavuto a Yuda. (mwachitsanzo Ezek 18:19-23; Dan 9:1-19)

3. Ndi chiyani chomwe anachisowa kwambiri nthawi ya ukapolo?

Anafunitsitsa mzinda wa Yerusalemu ndi Nyumba ya Mulungu zomwe zinkafanizira Mulungu pa dziko la pansi pano. (Mwachitsanzo Dan 1:1-7; 6:10; 9:1-3, 12, 16; 2 Mbi 5:13-14)

4. Kodi Mulungu adasamalira anthu ake ku ukapolo?

Inde, Mulungu anasunga anthu ake komanso a mbanja la Davide kukhala ndi moyo.

5. Perekani chitsanzo cha momwe Mulungu anasamalira anthu ake.

Inde, Mulungu anamsunga Daniele amene anali wokhulupirika ndi anzake ena atatu.

6. Izi zinawoneka bwanji?

Daniele ndi anzake atatuwo anawakweza kukhala akuluakulu a ku Babiloni. (Dan 2:47-49; 3:30; 6:1-3)

7. Kodi adakomana ndi mavuto ena ali onse chifukwa chowopa Mulungu?

Inde, anzake a Daniele anawaponya mn'ganjo ya moto, ndipo Daniele anamponya mphanga la mikango koma Mulungu anawapulumutsa. (Dan 3:19-23; 6:10-24)

8. Kupatulapo Daniele, ndi mneneri wina uti amene anagwira ntchito yake nthawi ya ukapolo?

Mneneri Ezekiele. (Eze 1:1-3)

9. Ezekiele anawatonthoza bwanji ana ake a Mulungu?

Powauza kuti Mulungu sakondwera ndi imfa imfa ya munthu wochimwa. (Eze 18:23, 32, 33:10-11)

10. Ukapolo unatha nthawi iti?

Nthawi yomwe Cyrus anakhala mfumu ya ku Persiya. (Eza 1:1-4)

*Vesi loloweza pamtima**:*** Eze 33:11

Uwauze kuti ine Ambuye Chauta ndikuti, Ndithudi, pali ine ndemwe, sindikondwa ndikaona munthu woipa alikufa. Ndikadakonda kuti aleke kuchimwako kuti akhale ndi moyo. Inu aIsraele, muferanji?Tembenukani, lekani zoipa zimene mukuchita.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO: 24
KUBWERERA KUCHOKA KU UKAPOLO

1. Chifukwa chiyani Mfumu Cyrus anawalora a Isaraele kubwerera ku Kanani?

Mulungu adamuitana Cyrusi ndi cholinga chomwecho ngakhale sanamudziwe Mulungu. (2 Mbi 36:22-23)

2. Kodi ndi onse anabwerera ku Kanani?

Ayi, koma anthu 50 000 okha ndiwo anabwerera ku Kanani? (Eza 2:64-65)

3. Ndani anawatsogolera akapolowa kubwerera kwawo?

Zerubabele, mwana wa mfumu. (Eza 2:1-2a; onaninso Hag 1:1)

4. Anthuwo adachita chiyani atangobwerera ku Yerusalemu?

Adamanganso Nyumba ya Mulungu ndi mzinda wa Yerusalemu. (Eza 3:7-10)

5. Ndani adawathandiza kwambiri?

Ezara, amene anali mlembi ndi Nehemiya yemwe ankanyamula chikho cha mfumu. (Mwachitsanzo Eza 10:6-12; Neh 7:1-10)

6. Kodi ntchito yomanganso Nyumba ya Mulungu ndi mzinda wa Yerusalemu inali yophweka?

Ayi, aYudawa anali ndi adani ambiri omwe anafuna kulepheretsa ntchitoyi. (Mwachitsanzo, Eza 4:1-10)

7. Ndi aneneri ati omwe analimbikitsa ntchitoyi kuti iyende bwino?

Hagai ndi Zakariya. (Mwachitsanzo Hag 1:1-8; Zak 4:1-10)

8. Kodi adawachenjeza makamaka za machimo ati?

Kukwatira akazi achikunja ndi kuphwanya sabata. (Mwachitsanzo Eza 9:1-5; 10:1-5; Neh 13:15-22)

9. Nyumba ya Mulungu yomwe adamanga inali ya maonekedwe otani ?

Inali yosakongola ngati yomwe adamanga Solomoni; ndipo Likasa la Chipangano munalibemo. (Eza 3:10-13; Hag 2:3)

10. Kodi a Isaraele anakhalanso ndi mfumu ina?

Ayi, ngakhale Mulungu anasunga banja la Davide ndi moyo, sipanakhalenso mfumu ina yochokera mbanja limeneli. (Eza 8:2)

*Vesi loloweza pamtima**:*** Hag 2:6-7

Zimene ndikunena ine Mulungu Wamphamvu zonse ndi izi: Patapita nthawipang'ono ndidzagwedeza dziko la pansi, nyanja ndi mtunda. Ndidzagwedeza mitundu yonse ya anthu ndipo chuma chonse cha anthu chidzabwera, motero Nyumba imeneyi ndidzaidzaza ndi ulemelero waukulu. Ndikutero ine Mulungu Wamphamvu zonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
AYUDA ATABWERERA KWAWO

1. Mbiri imafotokoza za ndani aYuda atangobwerera ku ukapolo?

Mbiri ya Estere yemwe anali mfumukazi ya mfumu ya ku Pesia. (Est 2:5-7, 15-17)

2. Mulungu adamugwiritsa ntchito yotani Estere?

Kusamalira zidzukulu zonse za Davide pamene Hamani woipa uja adafuna kupha aYuda. (Est 3:13 – 4:10; 6:14 – 7:7; 8:5-12)

3. Mneneri wotsiriza ndiye yani?

Malaki, amene anakhalapo zaka 400 Ambuye Yesu asanabadwe.

4. Malingana ndi Malaki, kodi Ayuda adatumikira Mulungu mokhulupirika atachoka kuukapolo?

Ayi, aYuda adachimwirachimwirabe. (Mwachitsanzo Mal 1:1, 7-9)

5. Kodi a Yuda anakhala amfulu patapita nthawi?

Ayi, anthu amitundu ina yamphamvu inali kuwalamulira. (mwachitsanzo Lk 3:1; Yoh 19:12)

6. Kodi anthu amitundu ina amenewa anawalamulira bwino A Yudawa?

Ayi, inali nthawi ya masautso ndi kuzunzidwa koopsa kwa ana a Mulungu.(Yer 24:7-10, 25:34)

7. Kodi analipo ena amene anali wokhulupirika kwa Mulungu?

Inde, awa anali kudikilira ndi chiyembekezo kudza kwake kwa Khristu. (Mwachitsanzo Yesaya 60:1-3; Yer 24:1-7)

8. Kodi Mulungu adakonzekera bwanji kubwera kwake kwa Khristu?

Iye adalora chi Giliki, chomwe ndi chilankhulo cha m'Chipangano cha Tsopano, kuti chikhale chilankhulo cha dziko lonse la pansi.

9. Ndi kagulu kanji koipa komwe kanakhazikika ku Israeli nthawi imeneyi?

Gulu la a Farisi amene ankakhulupira chipulumutso chifukwa cha ntchito zabwino. (Mt 5:20; 12:1-8 ndi ena)

10**. Ndi mtundu uti omwe unakhala ndi mphamvu zambiri pakutha pa nthawi imeneyi?**

Aroma, omwe ankalamulira dziko la pansi pamene Khristu anabadwa. (Lk 2:1)

*Vesi loloweza pamtima**:*** Malaki 3:1

Mulungu Wamphamvu zonse akunena kuti, "Ndidzatuma wamthenga wanga kuti akandikonzere njire. Kenaka mwadzidzi Mulungu amene mukumfunafuna adzafika ku Nyumba yake. Wamthenga wa chipangano amene mukumuyembekeza, suuyu akubwera".

Copyright © Gratia Dei Sola Media